ttb_Nya_0837_script

**2 Atesalonika : 1:10-2:9**

**Mutu : Tsiku la Ambuye**

Ndipereka moni kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero Ambuye atitsogolere ndi mau apa Chibvumbulutso 22:17, amene akuti, “Ndipo Mzimu ndi mkwatibwi anena, idzani. Ndipo wakumvaludzu adze; iye wofuna, atenge madzi a moyo kwaulere.”

Tsono mupologalamu yapita tinali kukambirana pa 2 Atesalonika 1:4-12, pamene timaona nkhani ya mazunzo, Kumwamba ndi Gahena.Ndipo lero pa 2 Atesalonika 1:10-2:9, tikambirana nkhani ya Tsiku la Ambuye.

**2 Atesalonika 1:10-12**

10. Pamene adzadzakudzalemekezedwa mwa oyera mtima ake ndi kukhala woyamikiridwa ndi onse wokhulupirira (pakuti mudakhulupirira umboni wathu tidauchitakwa inu) m’tsiku lija.

Paulo pano akunena kuti pobwera Ambuye Yesu padziko lapansi patsiku lachiweruzookhulupirira kapena kuti oyera mtima

onseadzamulemekeza Kristu.Kunena kuti tsiku limenelo Yesu amene ananyozedwa ndi anthu osakhulupiriraadzalemekezeka. Tsiku limenelo Yesu adzalemekezedwa ndi anthu oyera mtima chifukwa adzawonaulemelero wake ndi kuwona ukulu ndi mphamvu yake. Tsiku limenelo oyera mtima adzawona chigonjetso cha Ambuye Yesu ndipo Yesu Khristu adzalemekezedwa mwa onse oyera mtima.

Tsiku lobwera Ambuye chisomo chake ndi mphamvu yake idzawonekera kudzera mwa anthu amene adawapulumutsa.Mphamvu yake idzawonekera pomwe osakhulupirira onse adzalangidwa.

11. Chomwechonso tikupemphereraninso nthawi zonse, kuti Mulungu wathu akakuyeseni inu oyenera kumayitanidwe awa, ndikukwaniritsa chokoma chonse cha ubwino wake ndi ntchito yachikhulupiriro ndi mphamvu;
12. Kuti dzina la Ambuye wathu Yesu Khristulilemekezedwe mwa inu, ndi inu mwa Iye, monga mwa chisomo cha Mulungu wathu ndi Ambuye Yesu Khristu.

Pano Paulo akuwuza Atesalonika kuti amawapempherera nthawi zonse.Ngakhale sanali pakati pawo komabeamawakumbukira.Ichi, ndi chinthu chopambana kwambiri chimene inu mungachitire ena.Kupemphelera ena kumasonyeza kuti umawafunira zabwino anzako.Tawonaniuwu, ndiwo unali moyo wa Paulo kupempherera Atesalonika. Kodi inu mulinawo mtima uwu?

Tamvani Paulo akunena kuti dzina la Ambuye wathu Yesu Khristulilemekezedwe mwa inu.Tidayitanidwa ndi Mulungu kuti tiyende moyo wachiyero. Tidayitanidwa kuti tichoke ku m'dima ndikuyenda ndi Ambuye mu ufumu ndi ulemelero wake.Tikuyenerakuyendamolemekeza dzina la Yesu Khristu Ambuye wathu. Tiyenera kupemphera kuti tikayendemolemekeza Ambuye Yesu chifukwa mwa ife tokha tilibe chimene chingatiyenerezekuyendamolemekeza dzina la Ambuye. Tisowa kuti Ambuye mwini wake amene adatiyitanaatipatse mphamvu yotitikayendemolemekezadzina lake.

Ndikukwaniritsa chokoma chonse cha ubwino wake ndi ntchito yachikhulupiriro ndi mphamvu: Chokoma chonse cha ubwino

wake ndi ntchito yachikhulupiriro zimachokera ku chisomo cha Mulungu. Kutanthauza kuti Paulo amapemphera kuti ntchito ya chisomo cha Mulungu ikapitilirekuwonekera mu ntchito zawo zonse.Ntchito yachikhulupiriroimagwirika mu mphamvu ya chisomo cha Mulungu. Ntchito imene ingalemekeze ndi kuwonetsa mphamvu ya chisomo cha Mulungu imachokerakwa Mulungu amene amayigwira kufikira kuyimaliza mwa onse amene amakhulupirira Mulungu.

**2 Atesalonika 2**

1. Ndipo tikupemphani abale, chifukwa cha kudza kwake kwa Ambuye wathu Yesu Khristu, ndi kusonkhana pamodzi kwathu kwa Iye

Paulo akunena kuti pobwera Ambuye wathu Yesu Khristuokhulupiriraadzasonkhana pamodzi ndi Iye. Kutanthauza kuti kudzakhalamkwatulowa mpingo. Apa Paulo akulembamowakumbutsa zimene adalembam'kalata yoyamba kukhudza zakubwera kwa Yesu patsiku la mkwatulo. Pa 1 Atesalonika 4:17 adalemba kuti;"Ife wokhala ndi moyo wotsalafetidzakwatulidwa nawo pamodzi m'mitambo, kukakomana

ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo poterotidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse.”Pachifukwa ichi okhulupirira ayenera kukhala mosagwedezeka ngati kuti zinthuzi zikuchitika.

2. Kuti musamagwedezeka mtima msanga ndi kutaya maganizo anu, kapena kuopsedwa, mwa mzimu kapena mwa mawu, kapena mwa kalata, monga wolembedwa ndi ife, monga ngati tsiku la Ambuye lafika.

Paulo akudandaulira Atesalonika kuti asagwedezeke ndi kalata imene sinalembedwe ndi atumwi.Kalata imene idali pakati pawo yomwe mudalembedwa zinthu zabodzazonamiza anthu kuti tsiku la Ambuye lidafika kale.Apa Paulo akuwawongolera Atesalonika mowadandaulira kuti asagwedezeke.

Ambuye adzabwerakudzaweruza dziko lapansi mosakayika konse. Ambuye Yesu adzabwera mu ulemelero wake patsiku lomaliza. Anthu ena amakayikira za zimene zidzachitike koma chinthu chimodzi chodziwikamosakayikitsa ndichakuti Ambuye Yesu adzabwera.

Mtumwi Paulo akuchenjeza a Atesalonika kuti sayenera kukhala ogwedezeka za nthawi yakubwera kwa Ambuye.  Anzanga kukhala

ogwedezekakumafooketsa chikhulupiriro.Anthu amene chikhulupiriro chawo chiri chofookaamanyengedwa ndi aneneri abodzamosabvuta.Musakhale ogwedezekam'chikhulupiriro kuti wina aliyense asakunyengeni.Tiyenera kukhazikika pa chimene Mau a Mulungu akunena kuti wina angatinyenge.

"Kapena kuopsedwa, mwa mzimu kapena mwa mawu, kapena mwa kalata."Malinga ndi mau awa, zikuwoneka kuti analipo wina amene amanamiza Atesalonika za Tsiku la Ambuye.Amawanamiza kuti tsiku limeneli lidafika kale.Alipo anthu ena amene amadziwonetsera ngati Mulungu amalankhula nawo mwapaderakuposera zimene Mulungu adalankhulam'Mau ake.Anthu oterewasawerenga mau a Mulungu.Amangokamba za maloto awo ndikumanena kuti ali ndi masomphenya apadera. Ndikosabvutakufalitsa maganizo ndi maloto athu ngati sitikuwerenga Mau a Mulungu.Ku Atesalonika kudafalitsidwauthenga wosiyana ndi Mau a Mulungu amene Paulo adawaphunzitsa.Izi zidayambakusokonezaokhulupirira.

Zikuwoneka kuti bodza limeneli lidachitakulembedwa ngati kalata.Kalata imeneyi idayambakuwerengedwa pakati pa

Atesalonika ndipo zolembedwa zake zimafalitsidwa pakati pawo ndikuyambakusokoneza maganizo ya okhulupirira.Kalatayoidalembedwamwachinyengochifukwa imakhala ngati kuti idalembedwa ndi Paulo, Timoteo ndi Silvano.

Kalatayo monga tanena kale imanena kuti tsiku la Ambuye lidafika kale.Chifukwa cha mazunzo amene Atesalonikawoamadutsamo ambiri mwa okhulupiriraadayamba kukhulupirira kuti kalatayo inali yowona.Amawona ngati alowa mu nyengo ya Chizunzo Chachikulu.

Tsiku la Ambuye lidzayamba ndi Chizunzo Chachikulu.Yoweli adafotokoza za Tsiku la Ambuye pa Yoweli chaptala 2. Petro adakumbutsa anthu za ulosi wa Yoweli za tsikuli pa tsiku la Pentekoste. Anthu panthawiyo amadziwa za Tsiku la Ambuye ndipo ena adayamba kuganiza tsiku la Pentekoste linali Tsiku la Ambuye. Pa Machitidwe 2:20 Petro adafotokozera za ulosi waYoweri: 'Dzuwa lidzasanduka mdima, ndi mweziudzasanduka mwazi, lisanadze tsiku la Ambuye, lalikulu ndi lowonekera.' Tsono ngakhale anthu amasokoneza Tsiku la Ambuye ndi tsiku la

Pentkoste mukhoza kuwona zimene zidachitika pa tsiku la Pentekoste sizimene amanena Yoweri. Patsiku lopachikidwakwa Yesu pa mtandakudagwa m'dima ndiponso kunachitika chibvomezi, koma zimenezinsosizimenezidachitika pa tsiku la Pentekoste.

Pa tsiku la Pentekoste, kudalibe mphepo koma mwadzidzidzi kudamvekamawu wochokera Kumwamba ngati mkokomowa mphepo yolimba, kudzaza nyumba yonse imene adalikukhalamo. Kudawonekera malilime wogawanika, wonga a moto; ndipo udakhala pa iwo onse wayekhawayekha. Ndipo iwoadadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayambakuyankhula ndi malilime ena, monga Mzimu adawayankhulitsa. Anthu adakhamukirakukachisikukawona chimene chimachitika.Petro pofotokozera adanena kuti zidachitika nthawi imeneyo ndizofanana ndi zimene Mneneli Yoweli adalosera.Petro adalongosola kuti anthuwo sanali ataledzera koma anali atadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Yoweli adanena kuti tsiku lina likubwera limene Mulungu adzathira Mzimu wake pa anthu onse, koma wonani kuti pa tsiku la Pentekoste Mzimu wa Mulungu sanathiridwe pa anthu onse

mwakuti amene sanathiridwe Mzimu amaganiza kuti enawo aledzera. Kusonyeza kuti Tsiku la Ambuye likubwera kutsogolo.

Petro adakambaponso za Tsiku la Ambuye kuti lidzafika usiku ngati mbala.Kumbukirani kuti pa 1 Atesalonika 5 tidawona kuti Ambuye sadzabwera kudzatenga Mpingo wake usiku ngati mbala. Mpingo uli maso kuyembekezera kubwera kw Ambuye. Koma kwa anthu osakhulupirira kubwera kwa Ambuye kudzafika usiku ngati mbala iwo akadalimtulom'machimo awo. Petro akupirizakufotoza motere pa 2 Petro 3:10: "Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala usiku; m'mene miyambaidzapita ndi chibumo chachikulu, ndi za m'mwamba zidzakanganuka ndi kutenthakwakukulu, ndipo dziko lapansi ndi ntchito ziri momwemo zidzatenthedwa.' Apa mukhoza kuwona kuti izinso zimene zidachitika pa tsiku la Pentekoste.

Tsiku la Ambuye likubwera ndipo ndi tsiku la chiweruzo kwa anthu osakhulupirira osati kwa mpingo. Akhristutikuyang'anira kubwera kwa Yesu mwa chiyembekezerochodala. Koma kwaosakhulupirira tsiku la Ambuye lidzakhalalowopsa monga akunenera pa

Chibvumbulutso 6:17: ‘Chifukwa lafika tsiku lalikulu la mkwiyo wake wafika, ndipo akhoza kuyima ndani.’

3. Munthu asakunyengeni kwina kulikonse, kuti tsikulosilifika, koma chiyambechifikechipatukochonabvumbulutsike munthu wosayeruzika, mwana wa chionongeko.

“Munthu asakunyengeni kwina kulikonse kuti tsikulosilifika.”Apa akunena za Tsiku la Ambuye osati za tsiku la mkwatulo. Tsiku la Ambuye silidzafika pokhapokha zinthu ziwiri izi zitachitika: Choyamba kudzachitika chipatukokutanthauza kuti chikhulupiriro chidzazima. Chachiwiri kudzabvumbuluka munthu wawuchimo amene ndi mwana wachiwonongeko. Ziwirizizidzayenera kuchitika Tsiku la Ambuye lisanafike.

Koma chiyambechifikechipatukocho: Chipatukokutanthauza kuti ambiri adzataya chikhulupiriro. Koma sikudzakhala kungotaya chikhulupiriro chabe komanso kuchoka pa njira ya chikhulupiriro.Chipatukochidzawoneka m’magulu awiri.Gawo loyamba mpingo wokhulupiriraudzachoka pa chikhulupiriro.Kutanthauza kuti chikhulupiriro cha abale

chidzazilala, anthu adzatayachikhulupiriro chawo.Gawo lachiwiri padziko padzakhala popanda chikhulupiriro m'pang'onong'ono pomwe.Anthu adzalekelatukupemphera. Gawo ililidzafika mpingo wa okhulupirirautakwatulidwa pa dziko lapansi. Choyamba chimene chidzachitike ndichakuti mpingo wa anthu okhulupiriraudzakhlautapatuka pa chowonadi. Chifukwa chakuchokakwa mpingo pa chowonadikudzakhalachipatuko mu mpingo. Tsiku la Ambuye ndi nyengo ya Chizunzo Chachikulu zidzayamba mpingo utadzapatuka pa chikhulupiriro.

Mpingo umene udzakhale pansi pano mkwatuloutachitikaudzachokeratu pachowonadi. Uku kudzakhalakupatuka pa chikhulupiliro. Ichi ndi chithunzi cha mkazi wachigololo chimene timawerenga pa Chibvumbulutso 17. Mpingo wa ku Leodikaya ndi mpingo wa chisanu ndichiwiri umene udalandirakalata m'buku la Chibvumbulutso ndipo unali womvetsa chisoni. Sunali wotentha kapena wozizira monga momwe mpingo uliri masiku ano.Okhulupiriraakadzatengedwa chikhulupiriro chidzatheratumum'pingo kotero kuti kudzakhalachipatuko.

Chachiwiri chimene chidzachitike ndichakuti munthu wawuchimo amene ndi mwana wachiwonongekoadzabvumbuluka. Akadzabvumbuluka munthu wauchimoChizunzo Chachikulu chidzakhala kuti chayambika.Munthu wauchimoyu ndi yemwe uja Yohane akumutchula kuti 'wokana Khristu.'Dzina lakuti "wokana Khristu' limapezeka m'buku la 1 ndi 2 Yohane basi.  Koma wokana Khristuali ndi mayina pafupifupi 30 m'Buku Lopatulika. M'Chipangano Chakale akutchulidwa kuti munthu wa Satana. Munthu waSatanayu adzalamulira ndikusokeza dziko lapansi. Munthu wa Satana akhoza kuti adafika kale pakati pathu koma mphamvu zake zidzawoneka pamene adzabvumbulitsidwe nyengo ya Chizunzo Chachikulu ikadzayamba.

4. Amene atsutsana nazo, nadzikuza pa zonse zochedwa Mulungu, kapena zopembedzeka, kotero kuti iye monga Mulungu wakhala pansi ku kachisiwa Mulungu nadziwonetsera yekha kuti ali Mulungu.

Munthu wauchimoyuadzayambakunamiza anthu kuti iyeyo ndi Mulungu.Pa Chibvumbulutso 13 tikumva za chilombochotulukam'nyanja (wokana Khristu)

adzayanjanitsamayiko ku madzulo.Akadzateroiyeyoadzayambakudzitchula kuti ndi Mulungu.Dziko lidzayesa kuti iyeyu ndi Yesu Khristu.Ichi chidzakhala chinyengo.

5. Simukumbukira kodi, kuti pokhala nanu, ndisanachoke ine, ndinakuuzani zinthu izi.

Paulo samazengereza kulankhula za chimene chili nkudza. Ena amatialalikiasamalalikire za zinthu izi. Paulo amalalikira Mau a Mulungu osachotsapo komanso osawonjezerapo.Tamvani akuwakumbutsa Atesalonika kuti akumbukiranizomweanawauza.

6. Ndipo tsopano chomletsamuchidziwa, kuti akabvumbulutsidwe iye m'nyengo yake ya iye yekha.

Kodi alipo amene akhoza kuletsachimo?Yekhayo amene akhoza kuletsachimo ndi Mzimu Woyera.Mayiko, maboma, ndi mabungwe sangathetse chimo.Mwinanso m'malo mothetsachimo ndi amene amalimbikitsa ufulu wauchimo.Boma la Aroma linali lankhanza.

7. Pakuti chinsinsi cha kusayeruzikachayambadi kuchita, chokhachi pa womletsa tsopano, kufikira a kam'chotsa pamenepo.

M'chitidwe wakusaweruzikakudayamba nthawi ya Paulo ndipo ukupitilira lero lino. Ambuye Yesu adaphunzitsa kudzera m'fanizo limene limawonetsanso momwe dziko lapansi liliri lero lino.Zinsinsinsi za Ufumu wa Kumwamba zimabvumbulutsa momwe dziko lapansi liriri. Mau a Mulungu akufesedwa masiku ano koma m'dani naye akufesanansongole.Tirigu ndi nansongoleakumelera pamodzi.Mau a Mulungu ndi nansongoleakukulira limodzi lero lino pa dziko lapansi.

Tsono kusaweruzika kukhala kukupitirirabe, koma Mzimu Woyera sakumulora Satana kuchita chifuniro chake chosaweruzika.Koma Mzimu Woyera akadzamulora Satana kuchita chifuniro chake pamenepo Satana adzamasuka kuchita kusaweruzika m'dziko lapansi.

8. Ndipo pamene adzabvumbulutsidwawosayeruzikayo amene Ambuye Yesu adzamuwononga ndi mzimuwa pakamwa pake, nadzamuwononga ndi mawonekedwe a kudza kwake.

Tsono pamene adzabvumbulutsidwawosayeruzikayoadzakhala wopanda womutsutsa padziko lapansi.Ambuye Yesu yekha akadzafika ndi amene adzamugonjetse. Monga ana a Isreali anali pamasautsoakulu ku Aigupto ndi momwenso okhulupiriraadzakhalire pansi pa ulamuliro wawosaweruzika wokana Khristu. KudzakhalaChizunzo kufikira Yesu atabwera kudzakhazikitsa ufumu wake.

Ambuye Yesu adzamuwononga ndi mzimuwapakamwa pake: Kutanthauza kuti Ambuye adzamugonjetsa ndi Mau ochokera pakamwa pake amene ali ngati lupanga lakuthwakonsekonse. Ndi Mau a Mulungu amene adalenga dziko lapansi. Mau a Mulungu ndi Malemba a moyo amphamvu.Ambuye Yesu pobweraadzabwera ngati Mau a Mulungu amoyo.

“Nadzamuwononga ndi mawonekedwe a kudza kwake.”Mawonekedwe a kudza kwake kutanthauzaulemelerowa kubwera kwake. Pa Tito 2:11 akunena kuti: “Pakuti chisomo cha Mulungu chimene chibweretsa chipulumutso chawonekera kwa anthu onse.” Kubwera kwake mu ulemelerokudzakhala kudzatenga okhulupirira kudzakhazikitsa ufumu wake. Anadza ku Betelehemu ngati mwana wakhanda, ndikuyamba utumiki wake ali ndi zaka makumi atatu pamene adapitandikuyeretsakachisi. Pobweranso kachiwiri adzabwerakoyambirira kukumana ndi mpingo wake mu mlengalenga ndipo pomalizaadzakhazikitsa ufumu wake. Panthawi imeneyo okana Yesu adzawonongedwa ndi mawonekedwe a kubwera kwake.

9. Ndiye amene kudza kwake kuli monga mwa machitidwe a Satana, mu mphamvu yonse, ndi zizindikiro ndi zozwizwa zonama.

Paulo pano akukamba za munthu wauchimo, wokana Khristu, munthu wosaweruzikawamachitidwe a Satana mu mphamvu yonse ya zizindikiro ndi zozizwa zonama.Munthu wosaweruzikayu adzakhala ndi mphamvu zodabwitsa monga kuchilitsa matenda.Kumbukirani kuti nthawi ya Yobu Satana adatumiza

mphepo imene idapha ana a Yobu psiti.Satana adzabwera ndi mphamvu ndi zozizwa. Pachifukwa ichi sitiyenerakuyika chikhulupiriro chathu pa anthu koma pa Yesu Khristu amene ndi woyamba ndi wotsiriza wa chikhulupiriro chathu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, munthu wosaweruzikayuadzafikandizizindikirozachinyengo, zonamiza anthu.Anthu pa dziko lonse lapansi adzayamba kukamba za munthu wosaweruzikayu.Anthu amene sakhulupirira Uthenga Wabwino adzakhulupirirazachinyengo ndi zonama za munthu wauchimowosaweruzikayu.

Lero tilekeza pano.Ndipo timasanthula2 Atesalonika 1:10-2:9, momwe tikambirana nkhani ya Tsiku la Ambuye.

Ambuye akudalitseni inu lero lino. Amen!